# Buku loyendetsera Alpha



# ZA MKATIMU


Kodi Alpha ndi chani? .......................... 2

Tipangirenji Alpha? .............................. 3

M'mene mungayendetsere Alpha ............... 4

Zinthu zisanu zoyenera kutsatira kuti muyambe ... 5

Lembetsani maphunziro anu a Alpha .......... 6

Chitsanzo cha momwe mungagawire nthawi ya Alpha ........................ 7

Chitsanzo cha phunziro la Alpha ........ 8

Pemphero ............................ 9

Kukhazikitsa gulu logwirizana ........... 10

Tingakuthandizeni bwanji? ............... 11




# KODI ALPHA NDI CHANI?

**Alpha ndi maphunziro omwe amatenga masabata angapo ndipo amachitika kudzera muzokambirana, kuunika za moyo wa chikhristu. Zonsezi zimachitika mowonetserana chikondi komanso molemekezana wina ndi nzake.**





**Palibe funso lomwe ndi losafunika. Palibe kupanikizika.**

**Chilichonse chomwe inu mumakhulupilira kapena kuganiza ndicholandiridwa.**

**Simukuyenera kulipira kalikonse - kukambirana zinthu za pamwamba ndi anthu oganiza mozama ngati inu, basi.**





# TIPANGIRENJI ALPHA?

**Alpha ndi ZENIZENI**
Onse omwe akuyendetsa maphunziro a Alpha timawalimbikitsa kukhala anthu opanga zinthu poyera komanso kukhala mu choona, chifukwa kutero kumapangitsa anthu ena omwe akubwera kudzachita nawo maphunzirowa kuti nawonso akhale omasuka ndikuwonetsera chenicheni chomwe iwo ali. Anthu amaloredwa kufunsa mafunso ndikupeza mayankho, palibe okakamizidwa kuti apereke maganizo ake komanso palibe kumulondola munthu ngati mwini wake wasankha kuti asabwerenso kumkumano wa Alpha.

**Alpha ndi YOLUMIKIZITSA**
Nsanamila yina yomwe Alpha idakhazikikapo ndiye kumanga ma ubale enieni omwe amapangidwa kwa masabata ochepa koma amakhala akupitilira kwa zaka zambiri.

**Alpha ndi YODALIRIKA**
Mu Alpha timadalira Mzimu Woyera, chifukwa timazindikira kuti ndi Mulungu yekha yemwe akhoza kusintha miyoyo ya anthu – ife timangothandizira kuti anthu amudziwe iye. Tikawalora anthu kuti akhale monga momwe iwo aliri komanso kufunsa mafunso omwe iwo alinawo, kuganizira zomanga ma ubale pakati pawo komanso kudalira pa Mzimu Woyera, miyoyo ya anthu ikhoza kusinthika.

**Alpha ndi YOBALA ZIPATSO**
Alpha imapereka danga kwa anthu wamba kuti athe kutenga nawo gawo pa ntchito yofunikira ngati imeneyi. Aliyense ali ndi kuthekera kupangitsa maphunziro a Alpha molumikizana ndi mpingo wake. Tawonapo nthawi zambiri kuti zinthu zina zomwe zimawoneka ngati zochepa kapena zosafunikira kweni kweni ndi zomwe zimatha kusintha zinthu maka maka mukaitana Yesu Khristu kuti akhale pakati panu.





# M'MENE MUNGAYENDETSERE ALPHA

**N'kumano uli wonse wa Alpha umadziwika ndi nsanamila zitatu:**





### 1 UCHELEZA ALENDO

Pa zochitika-chitika zambiri pamayenera pakonzedwe chakudya kapena zakumwa zoziziritsa kukhosi. Mu maphunziro a Alpha, timakhulupilira kuti chakudya chimathandiza kubweretsa pamodzi anthu osiyanasiyana, omwenso amakhala ali ndi mafunso osiyanasiyana, malingaliro osiyanasiyana okhuza moyo, ndipo anthuwa amakhala akugawana chakudya kwinaku akuchezerana ndi kudziwana bwino bwino.





### 2 KUMVETSERA MAPHUNZIRO

Ikatha nthawi yolandira chakudya komanso yodziwana wina ndi nzake, pamakhala kumvetsera maphunziro pang'ono kudzera mu kanema kapena kumvetsera munthu akulankhula nthawi yomweyo. Zolankhula zimenezi zimathandizira kuti anthu apitilire kukambirana fundo zikuluzikulu komanso zofunika pa nkhani ya chikhulupiliro. Nthawi zambiri makanema amenewa amakhala a mphindi makumi atatu (30). Zokambirana za Alpha zonse zilipo khumi ndi zisanu (15) ndipo zikhoza kuunikidwa mu masabata khumi ndi imodzi (11) kuphatikizapo tsiku la Alpha lomwe likhoza kukhala mkatikati mwa sabata kapena kumapeto kwa sabata.





### 3 ZOKAMBIRANA

Iyi ndiye nsanamila yayikulu ya maphunziro a Alpha. Uwu umakhala mwayi oti anthu agawane nzeru kudzera mukukambirana momasuka, komanso m'magulu a anthu ochepa omwe pakati pawo pali chikondi. Zokambirana zimenezi zimathandizira kuzamitsa chikondi pakati pa anthuwa ndipo zimawonetsera zipatso za moyo wa Chikhristu. Palibe amakakamizidwa kulankhula ngati sanafune kutero.

# ZINTHU ZISANU ZOYENERA KUTSATIRA KUTI MUYAMBE

**Dinani apa kuti mumvetsere ziphunzitso za Alpha**

1 **PEMPHERANI ndipo pitirizani kupemphera**
- Nthawi. Pemphelerani kuti muyambe Alpha munthawi yoyenera
- Gulu. Pemphelerani gulu loyenera loti lidzikumana ndi kutumikira limodzi
- Oyitanidwa. Pemphelerani omwe ayitanidwa kuti achimve mu mitima mwawo kuti nawonso akayesere Alpha

2 **KONZEKERANI NDI KULEMBETSA Alpha yanu**
Chili chonse chofunikira poyendetsa maphunziro a Alpha chilipo pa makina a intaneti ndipo ndi zaulere, mungolowa pa app.alpha.org/ssa
- Pitani pa MyAlpha uti muyambe kapena kulowa ngati munayamba kale
- Tsegulani Alpha yanu kuti mupeze zonse zofunikira pa maphunziro anu
- Tsatirani ndondomeko zili pa tsamba linalo ngati mungafune thandizo lina lirilonse

3 **TSITSANI zokambirana komanso zothandizira kuyendetsa gulu lanu**
- Mu MyAlpha dinani pa Alpha yemwe mwalembetsa
- Yang'anani mu zipangizo zophunzitsira (Series Materials)

4 **SANKHANI NDIPO PHUNZITSANI gulu lanu**
- Mu 'MyAlpha' pitani pomwe pali Malo Ophunzilira (Learning Centre) Unikani Alpha 101 komanso fundo zisanu ndi ziwiri (7) za kachitidwe kovomerezeka (7 Best Practices)
- Tsitsani komanso kuwonelera maphunziro a gulu laling'ono ndi gulu lanu, izi zili mu Zipangizo Zophunzitsira (Series Materials)

5 **LENGEZETSANI NDI KUYITANIRA**
- Mu 'MyAlpha' dinani pa Alpha yemwe mwalembetsa
- Pitani pomwe palembedwa Lengezetsani (Promote) kuti mupeze zonse zofunikira

Zatheka apa! **Mwakonzeka kuyamba ulendo wanu** wa Alpha, ndipo ife tilipano kukuthandizirani. Ndichikhumbokhumbo chathu kulumikizana nanu komanso kupemphera nanu choncho tilankhuleni.

Ngati mukufuna kudziwa zambiri, **pitirizani kuwerenga**.

**DINANI APA KUTI MUYAMBE**

# LEMBETSANI MAPHUNZIRO ANU A ALPHA

Chilichonse chomwe mungafune kuti muyendetse maphunziro a Alpha chilipo kudzera pa makina a intaneti ndipo ndi zaulere. Pitani pa: app.alpha.org/ssa.

Mukafuna thandizo lina lirilonse, tilankhuleni pa africa@alpha.org.

**M'mene mungayambire:**

1. Pitani pa MyAlpha kuti muyambe ndipo ndi zaulere: app.alpha.org/ssa

2. Ngati mukulowa koyamba, dinani pomwe pali mawu oti Sign Up

3. Lowetsani zina zofunikira, kenako pangani mawu achinsisi omwe mudzilowera nthawi zonse kapena mutha kulowa pogwiritsa ntchito zomwe mumalowera pa Google

4. Mulandira uthenga otsimikizira kudzera ku email kwanu. Pitani ku email kwanu mukawone ngati mwalandira uthenga ndipo dinani pa uthenga omwe mwalandirawo kuti mupitirize

5. Bwelerani ku MyAlpha, tsopano mutha kulowa mu akaunti yanu ya Alpha

**M'mene mungayendetsere maphunziro:**

1. Lowani mu MyAlpha (Ngati mukuyamba kumene tsatilani ndondomeko zomwe zili pamwambapo)

2. Pa Dashboard, dinani mawu ofira oti Register new Alpha pamwamba pafupi ndi pa kona chaku manja kwanu

3. Onerani maphunziro onse omwe alipo ndipo kenako sankhani zomwe inu mukufuna muphunzire.

4. Yankhani mafunso angapo okhudza Alpha yanu, monga:

Alpha yanu mukupangira ndani? Mukufuna maphunziro akhale muchilankhulo chanji? (Ngati mukufuna maphunziro anu akhale muzilankhulo zingapo, lembetsani maphunziro anu mu zilankhulo zonsezo)

5. Lembani zofunikra za Alpha yanu (tsiku loyambira, mpingo/bungwe), bweleranimo zomwe munapanga koyambilira ndipo ngati zonse zili bwino lembetsani maphunziro anu

- Mpingo/Bungwe: Ngakhale kuti maphunziro anu simukupangira ku tchalitchi komabe tchulani mpingo omwe inu mumapemphera. Izi zimatithandizira kudziwa kuti ndi ndani akupangitsa maphunzirowa mu tchalitchi, kunyumba, mumashop, ndi malo ena otero komanso ngati pali kachitidwe kosiyana ka zinthu mu mipingo yina. Nthawi zina pamakhala anthu anayi kapena asanu oti amapita ku mpingo umodzi koma amapangira maphunziro a Alpha kunyumba!

6. Muzakumbutsidwa kuti mulengezetse maphunziro anu a Alpha kudzera pa intaneti. Ngati Alpha yanu ndi yoti aliyense atha kutsegula, onesetsani kuti mwalemba dzina la Alpha yanu, Email yoti mukhoza kupezerako mauthenga, malo omwe mumapangira Alpha yanu, tsiku lomwe munayambira ndi cholinga choti anthu akhoza kupeza Alpha yanu mosavuta.

- Alendo onse akamalowa mu Alpha yanu, mudzilandira uthenga kudzera ku email yanu. Zikatere, mukhoza kuwatumizira mauthenga ambiri ofunikira monga keyala yanu, komwe mumakumana kapena m'mene mungakumanilane kudzera mu njira zamakono monga pa Zoom, ndi zina zambiri.

- Ngati Alpha yanu ndiyosafikirika ndi munthu wina aliyense kapena kuti ndiyotseka, kapena tsiku lomwe munayambira silinatsimikidzike, mukhoza kumatsegula kwa kanthawi ndi kutsekanso.

- Mukasankha Make your Alpha public ndiye kuti maphunziro anu aziwonedwa ndi wina aliyense amene angakhale akusaka maphunziro a Alpha akalowa pa alpha. org/try-alpha. Ganizirani mozama popanga chiganizo chimenechi kuti ndi bwino kutero kapena ayi kutengera ndi momwe inu mukuwonera.

7. Apa tsopano mutha kupeza ma kanema a Alpha, ziphunzitso, mafunso a m'magulu a anthu ochepa kuyitana alendo ndi zina zambiri. Zonsezi ndi zaulere ndipo zikupezeka kudzera pa intaneti!

**M'mene mungapezere zipangizo zonse:**

1. Mukangolembetsa maphunziro anu, dinani pomwe pali MyAlpha Courses kuti muwone zonse zomwe muphunzire

2. Dinani View and edit kuti mutsegule zomwe muphunzire. Mukatsegula phunziro lanu, dinani Schedule kuti musinthe nthawi kapena m'mene mukufuna kupangira maphunziro anu

3. Dinani Promote Kuti mupeze mauthenga ndi zipangizo zina zothandizira kulengezetsa maphunziro anu a Alpha ku mpingo wanu ndi kuwapatsa kuthekera kuti athe kukuyitanirani alendo kuzapanga nawo maphunziro a Alpha. Pali zinthu monga ma poster, ma khadi oyitanira alendo, uthenga wapa masamba amchezo komanso ma kanema.

4. Dinani Series Materials kuti mupeze zinthu zinanso zambiri monga zothandizira pa maphunziro, makanema, ndi zina zambiri zofunikira pa maphunziro a Alpha

5. Dinani Team kuti muitane gulu lanu kuti liwone m'mene mwakonzera maphunziro anu ndi zina zonse zofunikira

# CHITSANZO CHA MOMWE MUNGAGAWIRE NTHAWI YA ALPHA

## Alpha Film Series
(Alpha wapa kanema)

Sabata yoyamba – Pali zina zokhuza moyo kuposera apa? (Mwambo okhazikitsa)

Sabata ya chiwiri – Kodi Yesu ndi ndani? Sabata ya chitatu – N'chifukwa chani Yesu anafa?

Sabata ya chinayi – Ndingakhale bwanji ndi chikhulupiliro? Sabata ya chisanu –Chifukwa chani ndipo ndidzipemphera bwanji?

Sabata ya chisanu ndi chimodzi – Chifukwa chani ndipo ndingawerenge bwanji Baibulo?

Sabata ya chisanu ndi chiwiri – Mulungu amatitsogolera bwanji?

**Kuphunzira za Mzimu Woyera**

Kodi Mzimu Woyera ndi ndani?

Kodi Mzimu Woyera amatani?

Ndingadzadzidwe bwanji ndi Mzimu Woyera?

Ndingatani kuti ndikhale wangwiro moyo wanga wonse?

Sabata la chisanu ndi chitatu – Ndingazembe bwanji tchimo?

Sabata la chisanu ndi chinayi –Chifukwa chani ndipo ndingawauze bwanji ena?

Sabata la khumi – Kodi Mulungu akuchiritsabe mpaka lero? Sabata la khumi ndi chimodzi – Tikutinji za mpingo?

Mwambo Okhazikitsa umakhala ngati chisangalaro, mwayi okambirana modekha momwe maphunziro a Alpha ayendere masabata angapo akubwera kutsogolo. Popeza sabata yoyamba ndiyosiyanako ndi masabata ena, mu sabata imeneyi simukhala nthawi yambiri yokambirana. Sabata imeneyi kwambiri yimakhala nthawi yoti anthu adziwane. Zokambirana zambiri zimakhala mu masabata otsatira.

## Alpha Youth Talks Africa
(Alpha wa Achinyamata mu Africa)

Sabata yoyamba - Moyo: Basi ndi omwewu? (Mwambo okhazikitsa) Sabata yachiwiri - Yesu: Kodi Yesu ndi ndani?

Sabata yachitatu - Mtanda: N'chifukwa chani Yesu anafa? Sabata ya chinayi - Chikhulupiliro: Ndingakhale bwanji ndi chikhulupiliro?

Sabata ya chisanu - Pemphero: Chifukwa chani ndipo ndidzipemphera bwanji?

Sabata ya chisanu ndi chimodzi - Baibulo: Chifukwa chani ndipo ndingawerenge bwanji Baibulo?

**Kuphunzira za Mzimu Woyera**

Mzimu – Mzimu Woyera ndi ndani ndipo amatani?

Kudzadzidwa – Ndingadzadzidwe bwanji ndi Mzimu Woyera?

Moyo watsopano – Ndingatani kuti ndikhale wangwiro moyo wanga wonse?

Sabata ya chisanu ndi chiwiri - Tchimo: Ndingazembe bwanji tchimo?

Sabata ya chisanu ndi chitatu – Kudziwitsa ena: Chifukwa chani ndipo ndingawadziwitse bwanji ena?

Sabata ya chisanu ndi chinayi - Machiritso: Kodi Mulungu akuchiritsabe mpaka lero?

Sabata ya khumi - Mpingo: Tikutinji za mpingo?

## Alpha Youth Series 2024
(Alpha ya Achinyamata ya 2024)

Sabata yoyamba – Kulandiridwa ku zokambirana (Mwambo okhazikitsa)

Sabata yachiwiri – Yesu ndi...?

Sabata ya chitatu – Kodi chikondi chenicheni chimawoneka bwanji?

Sabata ya chinayi – Ndi chifukwa chani ndingafune ubale ndi Mulungu?

Sabata ya chisanu – Kodi ubale ndi Mulungu umawoneka bwanji?

**Kuphunzira za Mzimu Woyera**

Kodi Mzimu Woyera ndi ndani?

Ndingadzadzidwe bwanji ndi Mzimu Woyera?

Sabata ya chisanu ndi chimodzi – Mulungu amatithangatira bwanji kugonjetsa tchimo?

Sabata ya chisanu ndi chiwiri – Kodi Mulungu akuchiritsabe mpaka lero? Sabata ya chisanu ndi chitatu - China chichitike ndi chani?

# CHITSANZO CHA PHUNZIRO LA ALPHA

Mukhoza kusintha kuti zigwirizane ndi gulu lanu.

## Alpha Film Series
(Alpha wapa kanema)

**OLA LIMODZI NDI MPHINDI 30**

Ola limodzi nthawi isanakwane – Kukonza pa malo

Mphindi 30 nthawi isanakwane – Kukumana komanso kupemphera

**ALPHA IKUYAMBIKA**

Mphindi 15 – Anthu oyitanidwa akufika ndi kuzungulira zungulira

Mphindi 20 – Kulandira chakudya

Mphindi 5 – Masewera ochangamutsa thupi

Mphindi 40 – Kumvetsera phunziro la Alpha komanso kukambirana

Mphindi 10 – Mwambo otseka

**KUMALIZA ALPHA**

Mphindi 15 – Gulu loyendeta Alpha kukambirana momwe zayendera

## Alpha Youth Series
(Alpha wa Achinyamata)

**PHUNZIRO LA MPHINDI 55**

Mphindi 10 nthawi isanakwane – Zokonzekera

**ALPHA IKUYAMBIKA**

Mphindi 10 – Alendo oyitanidwa akufika, kudyera limodzi, kucheza ndi kuzungulira zungulira

Mphindi 5 – Kulandira anthu (alimbikitseni kuti akhoza kuyamba kudya)

Mphindi 35 – Kumvetsera phunziro la Alpha

Mphindi 5 – Mwambo otseka

**KUMALIZA ALPHA**

Mphindi 10 – Gulu loyendeta Alpha kukambirana momwe zayendera

## Alpha pa Intaneti

**PHUNZIRO LA OLA LIMODZI NDI MPHINDI 15**

Mphindi 20 nthawi isanakwane – Oyendetsa Alpha kukonzekera, kupemphera komanso kuwonesetsa kuti makina onse akugwira bwino ntchito

**ALPHA IKUYAMBIKA**

Mphindi 5 – Kukumana ndikupatsana moni komanso kulandirana

Mphindi 10 – Kucheleza alendo kwa pa intaneti

Mphindi 30 – Kumvetsera phunziro la Alpha

Mphindi 30 – Zokambirana za m'magulu a anthu ochepa

**KUMALIZA ALPHA**

Mphindi 10 – Gulu loyendeta Alpha kukambirana momwe zayendera

# PEMPHERO

**Pemphero lofunika mkatikati mumaphunziro oyambilira**

Kutengera phunziro la Alpha lomwe mukuwonera, pomaliza pakhoza kukhala pemphero lalifupi kuchokera kwa m'modzi mwa anthu omwe akutsogolera maphunziro. Izi zimapereka mwayi kwa anthu omwe ayitanidwa kuti atha kupemphera mwachinsinsi ngati angafune kutero.

**Phunziro la chisanu ndilokhuza Pemphero**

Pa nkhani ya pemphero, timalimbikitsa kukambirana m'magulu a anthu ochepa kenako pamapeto kuyesera kupemphera limodzi. Omwe akuchititsa maphunziro akhoza kupemphera pemphero lalifupi chabe kapena kupereka mwayi kwa m'modzi mwa anthu oyitanidwa kuti apemphere mokweza. Pakapita masabata angapo, omwe akuchititsa maphunziro akhoza kusankha kuti maphunziro a m'magulu onse adzitsekedwa ndi pemphero.

Dziwani: Mu maphunziro a Alpha, timalimbikitsa kuti MUSAMAPEMPHERE musanalandire chakudya kapena nthawi yomwe mukupanga maphunziro ogawana m'magulu mpaka kufikira sabata ya chisanu. Izi zimathandizira kuti kudzera m'magulu ang'ono ang'ono anthu akambirane kaye mozama zokhudza nkhani ya pemphero.

**Kupemphelera anthu ena omwe ali pafupi kumaliza maphunziro a Alpha**

Mwambowu kawiri-kawiri umachitika mukakhala kuti mukuyandikira kumaliza maphunziro anu a Alpha. Uwu ndi mwayi oti munthu apumule ku ntchito za tsiku ndi tsiku ndipo munthu umakhala ndi mpata olingalira, osangalala limodzi ndi anzake, kudziwa zambiri za Mulungu komanso ngati ndiokonzeka kuyamba moyo wokhala m'pemphero. Ziphunzitso zakumapeto zimayima kwambiri pa nkhani ya Mzimu Woyera – kodi iye ndi ndani, chifukwa chani, ndipo amatithangatira bwanji kuti tisachoke pamaso pa Yesu Khristu komanso kuti tikhalebe naye pa ubale. Tikafika pa mapeto, alendo onse oyitanidwa amakhala ndi mwayi opemphera komanso kupempheleredwa ndi omwe akuyendetsa maphunziro kapena othandizira. Timafuna tipereke mwayi kuti anthu omwe ayitanidwa awone chikondi cha Mulungu kudzera mwa Mzimu Woyera.

**Pemphero ndi Machiritso**

Kumapeto kwa phunziro la machiritso, timalimbikitsa m'magulu a anthu ochepa kukambirana za nkhaniyi komanso pomaliza kupemphelera machiritso. Ndi nthawi ngati iyi ya mapemphero pomwe Mulungu amapanga zinthu zodabwitsa ndipo amakhala akukhuza mitima komanso matupi athu. Mulungu amakonda kuwonetsera ukulu wake kwa anthu omwe amafunafuna nkhope yake ndipo mu chowonadi.







# KUKHAZIKITSA GULU LOGWIRIZANA

Kukhala m'modzi mwa anthu oyendetsa Alpha ndi chinthu chopindulitsa komanso chonyaditsa kwambiri kwa munthu ogwira ntchitoyi modzipereka. Anthu omwe ali ndi zochita komanso kaganizidwe kofanana amatha kubwera pamodzi ndi kupeza abwenzi, kupititsa patsogolo luso lawo komanso kuphunzira kugwira ntchito limodzi. Gulu logwirizana ndi lofunika kwambiri chifukwa likhoza kupereka chithunzithunzi chabwino kwa alendo omwe ayitanidwa kudzakhala nawo pa maphunziro a Alpha.

**OYENDETSA NDI OTHANDIZIRA**
Ndi anthu achikondi ndi anzawo, ochita zinthu mwadongosolo komanso kuchita zinthu poyera?

**KUCHELEZA ALENDO**
Ganizirani anthu omwe mukuwadziwa kuti amakonda komanso ali ndi mphatso yocheleza alendo. Zingawoneke bwanji mutayitana anthu oterewa kuti akathandizire kukonza chakudya kapena kuthandizira kupeza njira zochelezera alendo kudzera mu njira zamakono monga pa makina a intaneti?

**KUYITANA ANTHU**
Amene angapeze njira zokonzera malo omwe mumakumaniranapo kuti akhale abwino osangalatsa komanso achikoka ndi ndani? Ndi ndani angathandizire m'dera lanu kuyitana anzawo kumaphunziro a Alpha?

**NTCHITO ZOFUNIKA UKADAULO**
Ndi ndani angathandizire kuwonesetsa kuti muli ndi zipangizo zoyenera zojambulira ndi kumvetsera ma uthenga a mau ndi pa kanema? Ndi ndani amatha kugwiritsa ntchito njira zamakono zopangira nkumano monga pa Zoom? Pezani anthu ena omwe amakonda kuthandiza koma samafuna kuwonekera ku gulu.

**OLANDIRA ALENDO**
Anthu oyambilira kukumana ndi alendo oyitanidwa ndi omwe akulandira alendowo popereka moni komanso omwe amakhala pa tebulo lolembetsera. Pezani anthu omwe amakonda kusekelera amakonda kucheza komanso kulumikizana ndi anthu.





# TINGAKUTHANDIZENI BWANJI?

**Tikudziwa kuti kuyamba komanso kuyendetsa maphunbziro a Alpha ndizopereka mantha. Musakhale ndi nkhawa, ife tili pano kuti tikuthandizeni!**



Jambulani QR code kapena
Pitani pa alphacourse.africa
kuti mudziwe zambiri,
kapena titumizireni uthenga pa
Contact page.



**Chifukwa chache mukani**,
phunzitsani anthu a mitundu
yonse, ndi kuwabatiza
iwo m'dzina la Atate, ndi
la Mwana, ndi la Mzimu
Woyera

Mateyu 28:19

www.alphacourse.africa